S. 3 Gwengwe: Brought up under traditional customs.

Kukula Ndi Mwambo

J. W. Gwengwe



KUKULA NDI MWAMBO

JOHN W. GWENGWE

LIMBE
MALAWI PUBLICATIONS AND
LITERATURE BUREAU
1970

Copyright © John W. Gwengwe, 1965

First published 1965
Reprinted 1970

Malawi Publications and Literature Bureau
Limbe, Malawi

Published by Macmillan and Co., Ltd., London
PRINTED IN HONG KONG
BY THE CONTINENTAL PRINTING CO. LTD.

MAU OYAMBA

Tsopano paoneka kuti papita zaka zambiri ife anthu ambiri tikadali ndi mtima wosakhala ndi chidwi, kufuna kufukula zina ndi zina zakale za makolo athu, maka-maka zolinga kufuna kudziwa zonse zokhudza miyoyo yao, monga miyambo yao yonse yosiyana-siyana.

Chimene ife amakono tiyenera kudziwa ndi ichi kuti, mtundu uli wonse udziwika kawiri-kawiri ndi miyambo yao, makhalidwe ao, ndiponso zochita-chita zao. Chinanso ndiye kuti munthu ayenera kunyadira mtundu wache ndi kuuchitira ulemu. Tsono nkofunika kuti anthu aziphunzira za makolo ao akale monga nzeru zao, nchito zao, mkhalidwe wao, m'mene anali kusungira dziko lao, chipembedzo chao, zimene anali kuzikhulupirira kuti zinali ndi mphamvu, zosiyana-siyana, zimene anali kuchita pa ubwana wao, chirankhulidwe chao, ndi zina zotere.

Anthu ena olemba mabuku adayesa kulemba mbali imodzi yokha ya zakale zotere koma olemba zamphumphu zache akadali ochepa.

Inenso ndangoyesa kulemba izi ndi izo koma osati zambiri ai chifukwa odziwa mozama za izo ndi akulu-akulu ndithu ndipo ambiri a iwo safuna kuulula zambiri akuti aopa kululutsa zakalezo. Ena akuti popeza azikonda sangathe kumangokamba-kamba za izo. Mwina akuti aopa kuputa Azimu.

Kukula ndi Mwambo

Ine ndikhulupirira kuti tonse tikagwirizana kuchita kafuku-fuku wa zakale zamakolo zonse tidzathandiza kuti mtundu wathu udzakhale wodziwika muyaya. Ngati ndidzaona kuti bukuli anthu akondwera nalo, ndiri okonzeka kulemba zina zonse zimene pakadali pano ndayesa kuti siziyenera kulowa m'buku'li.

Ndiyamika Bambo S.Y. Nthara amene anawelenga buku'li nandirimbitsa mtima kuti nditumize kuti likalembedwe msanga. Iwowa anawerengapo bukuli nanenapo zina ndi zina za upangiri. Ndiyamika Bambo Fletcher Mtosa amane analemba pa "Type writer" buku lonse'li.

Cholinga changa chachikulu ndicho kuti ndidzalembe buku lina lalikulu kaya la masamba 300 kuti mtsogolo lidzakhale limodzi la mabuku owerengedwa ndi anyamata ndi atsikana ophunzira maphunziro a *Ukachenjede* kaya *Ukadaulo* kaya *Ulangizi* ku masukulu apamwamba (Universities monga *Bachelor's Degree*, *Master's Degree* ndi *Doctor's Degree*). Izi zonse zikhudza maphunziro ofunikira za anthu (Anthropology). Ndikhulupirira kuti pa zaka za mtsogolo, maphunziro athu a masukulu onse adzachitika m'chinenedwe chathu chathu monga amachita maiko ena, ndidziwa kuti padzapita zaka koma tsiku lina kudzatheka ndipo mabuku otere adzathandiza ndithu.

John W. Gwengwe.

ZA M'KATIMU

		Tsamba
	Mau Oyamba	iii
1.	Kalikokha ndi Banja Lache . . .	2
2.	Mbumba Ya Kalikokha ndi Dambudzo .	11
3.	Chiipirawachaje Aphunzitsa Mwambo Wa Chisuwani	15
4.	Makolo	19
5.	Katundu Apite Kwa Yani?	21
6.	Kupembedza Kwa Kale	23
7.	Chokolo	38
8.	Mwambo wa Nchito za Pa Banja Ndi Mwambo Woyenera Munthu Wokhwima Msinkhu . . . . . —makhalidwe abwino — nchito za manja —magule akale — zoimba-imba zakale —misampha — zobvala zakale —mawerengedwe akale — mankhwala —nyimbo zaubwana — zodzikometsera nazo zakale	39
9.	Ubwana ndi Unamwali . . .	61
10.	Maphunziro Akale	72
11.	Zingalume ndi Phulantenga Akula . .	74
12.	Nanthola, Mwasanya, M'meendo ndi Mpokosa Akula	77
13.	Mwambo wa Nchito zina . . .	93

14. Mwambo wa Chinamwali . . . 95
15. Misinkhu 101
16. Ulemu wa Mkazi ndi Mwamuna . . 103
17. Miyeso 104
18. Mabweredwe a Imfa Pakati Pa Anthu . 107
19. Imfa Zododometsa 109
20. Kubadwa Kwa Ana 110
21. Maloto 112
22. Malodza (Mipingu) 113
23. Maula 115
24. Mwabvi 125
25. Mdulo (Tsempho) 132
26. Nkhondondianansi Amwalira . . 135
27. Mwambo wa za ufumu : . . . 138
—malamulo a Zaufumu
—malamulo akale odziwika
—nyimbo zoponyera ufumu
28. Angadziwe izi Ndani ? 144
—tanthauzani izi 147


1. *KALIKOKHA NDI BANJA LACHE*

Kale-kale panali munthu wina dzina lache anali Kalikokha. Iyeyu kwao kunali ku Mtenjere. M'nthawi zimenzo panali nkhondo pakati pa Achewa ndi Angoni, iyeyu anali m'modzi wa ana a Angoni ndipo anangolowerera pamene anali kuthawa mipaliro yancheto yaulembe ya Achewa.

Nkhondo imene'yi inali kuchitika pa dambo lochedwa Mlodzambunyani pafupi ndi phiri lochedwa Mbirankhonkho.

Pamene Kalikokha anali wopho-wopho m'machire ndi m'ziyango-yango anakumana ndi zobvuta zambiri-mbiri. Sanapeza chakudya chokwana, ankangodya mpatsachiuno, mirusu, m'merambuzi, nziru, mchisu, nthenjere, tsutsumudya, yaya, mapoza, nsewe, mkundi ndi chiteta.

Mwadzidzidzi tsiku lina anangomva kulira kwa zoweta. Poyamba anamva kulira kwa nkhosa. Kalikokha anathamangira kumeneko ndipo atayenda pang'ono, anapeza gulu la nkhosa limene linali ndi abusa awiri Mirimbombo ndi Kamkondo. Kalikokha atatulukira pafupi, anyamata aja anamva kumina kwa nkhosa zija kuti, m'nfi ! m'nfi ! m'nfi ! Ndipo abusa aja anadziwa kuti pali chinthu kapena choopsya. Pamene anakweza maso ao, anayamba ndi Kamkondo kuona kalikokha. Kamkondo



Kalikokha ndi Dambudzo.

anadabwa kuona chinthu chonga munthu amene anali woonda koposa, kotero kuti sanakhulupiriranso kuti ndi munthu koma anayesa ndi m'zukwa kapena chidude. Pamene anaona kuti chinthucho chinali kuwathamangira Kamkondo anakuwa nati : " Mirimbobo ! Mirimbobo ! Tiyeko tithawe taona Chimzukwa icho ! "

Mirimbobo anati : " Iwe usathawe, nanga nkhosa'zi zitsala ndiyani ? Ndiponso sichirombo ai ndi munthu amene'yu, tiyeko tiime pompano. Ona, ali kubwera, ndi munthu usaope. Kodi iwe ndiwe mwamunadi weni-weni ? Mudzapweteka ndi njokaluzi."

Kalikokha anati : " Pepani anzanga musathawe ndine m'nzanu monga inu muli, ndafoka ndi njala, londolereni kumudzi kuti ndikalandire chakudya kwa achifundo."

Abusa aja pomuona anamva naye chisoni popeza anaona kuti thupi lache lonse nfundu ziri kholophethe, mitsempha iri waa ! tsitsi liri pepere-pepere, maso adalowa kale mkati, khosi liri sololoke ndi nthiti ziri ngumbala-ngumbala. Iwowa, anangokusa nkhosa zao kupita kumudzi pamodzi ndi Kalikokha.

Pofika kumudzi amene anayamba kukumika Kalikokha ndi mlongo wache wamkulu wa Kamkondo dzina lache Dambudzo. Dambudzo anali mwana wamkazi wachikhwimire ndi woyenera banja. Iye'yu

adachita tsoka kuti sanapalidwe ubwenzi msanga popeza sanali wokongola kweni-kweni, kotero kuti anzache onse anthanga imodzi anali atakwatiwa ndi kukwatira. Ambiri a iwo anali nchembere katatu ena kanai.

Dambudzo analota kuti mlendo uja ayenera kukhala nthola. Ndipo anachiyesera chanzeru kuti amusamale kuti mwina mtsogolo n'kudzabvomereza zija za konza kapansi kuti kam'mwamba katsike.

Dambudzo anati: " Achimwene, lowa naoni m'mphala mwanumo alendowo kuti mulandire chakudya." Pamene anamva mau awa, Kalikokha anali ndi chimwemwe koposa ndipo anangosekera kumbali ndipo mumtima mwache anabwera malingaliro aja akuti, laponda la mphawi.

Posachedwa atalowa m'mphala muja, Kalikokha anangomva mau pakhomo kuti, " Zikomo ! Zikomo ! " Pomvetsetsa anamva mau achikazi ndipo iye anayamba kuolobzya miromo yache kuti angachite manyazi popeza inali yothetheka ndi njala. Kamkondo anati: " Eee ! lowani ! " Dambudzo anati : " Sindirowa, ndirikuchita manyazi ndi anthuwo. Mundiperekereko moni, munenenso kuti tidzakondwera ngati akhala nafe nthawi yaitali." Dambudzo ananyamuka kukakonza chakudya.

Kalikokha pamene anamva zakulandiridwa kwa ufulu kotere, anayamba kulowa maganizo mu mtima wache aja a " buluzi akhumbira khonde ", ndipo

anayamba kufunsa mafunso. Anati : " Kodi iwe Kamkondo, amene'yu ndani ? "

Kamkondo : " Amene'yu ndi mlongo wanga, pamutu pachepa padaponda atatu ine ndine wachinai."

Kalikokha : " Kodi iye'yu ndi wokwatiwa ? "

Kamkondo : " Iai ngosakwatiwa moti aliripa ngolema popeza anzache onse achisewere chache adatha n'kukwatiwa ndipo adachembezanso."

Kalikokha : " Iye'yu ndithu ndamuona kuti ali ndi mtima wabwino ndi wachifundo ndipo ndaonanso kuti ali ndi mtima wosunga munthu."

Kamkondo : " Amene'yu ifenso amatidodometsa moti m'banja mwathu'mu iye'yu palibe wina woti n'kufanana naye pachikhalidwe. Anzache ena ndi amambala ndipo saopa amuna ai moti mirandu ingokhala iri tawa-tawa."

Kalikokha : " Koma ine Dambudzo'yu ndamkonda moti kukadakhala kotheka, ine ndikadamupala chibwenzi, koma ndiri ndi zobvuta ndi zoletsa zambiri."

Kamkondo : " Kodi za iwe ngati n'kubvutika ? Ndadziwa uli ndi malingalira a za chuma chothandizira mkazi amene ungapute'yo."

Kalikokha : " N'zoonadi, pazoterezi kwathu pamafunika mphotho za kulowolera mkazi, koma chisoni ine ndiribe."

Pamene anamva mau awa, Kamkondo anapita kwa

mlongo wache Dambudzo namuuza nati: " Kodi mwanva ? Alendowatu akuti akukondani ndipo akuti akadakhala wachuma akadakukwatirani." Dambudzo anati: " Auzeni kuti ine ndiribe nazo kanthu malinga ukwatiwo basi, ngati munthu amakwatiwa ndi chuma, koma munthu mnzache." Kamkondo anapita kwa Kalikokha namuuza zonse zimene mlongo wache analankhula ndipo Kalikokha analimbikitsidwa pa maganizo aja ofuna kukwatira Dambudzo.

Chakudya chitabwera, onse aja anadya chakudya chija, koma Dambudzo chifukwa cha manyazi anadyera payekha. Kalikokha anakondwera nacho chakudya chifukwa kansima kache kanali kophika bwino ndi konunkhira moto ndipo ndio zache zinali inswa kamchere kache kamene Dambudzo adathiramo, kanali koutsa mudyo. Kamkondo ndi abale ache ena, anadziwa kuti tindioto tidamukomera Kalikokha popeza kudya kwache kunali kolapira.

Zitatha izi, Kalikokha anayamba kupangana ndi abale ache a Dambudzo za ukwati. Bambo ndi mai wa Dambudzo atamva, anakondwera ndi mbiriyi. Onse a banja lija anadziwa kuti Kalikokha ndi m'mphawi motero sadafune kumchedwetsa kutenga Dambudzo kuti akhale mkazi wache. Atate a Dambudzo anatenga kanyumba kena kuti kakhale ka Kalikokha ndi mkazi wache.

Patapita miyezi ina mkazi wa Kalikokha anali ndi pathupi (wodwala) ndipo pambuyo pache anabala ana a mapasa amuna awiri Phulantenga ndi zingalume. Nanthola anabadwa patapita zilumita zina. Banja la Kalikokha linali ndi chikoka chifukwa cha makhalidwe a banjalo, linali chitsanzo, banja lopanda ndeu ndi bzyokolo-bzyokolo. M'mudzi m'mene munali kuchitika izi ndi mwa Kambironjo.

MAFUNSO


1. Kodi Kalikokha analikudya zakudya zotani m'chire ? Chulani khumi zokha.
2. Kodi zinthu izi n'ziyani ? :—
   Ziyango-yango, Ncheto, Mlodzambunyani, Kamkondo, Chidude, Nfundu, Njokaluzi, Nthola, Bzyokolo-bzyokolo, Zirumika ?
3. Fotokozani bwino bwanji Dambudzo sanakwatiwe msanga, nanganso mukudziwa bwanji za nthanga zache ?
4. Kodi Dambudzo anali wamakhalidwe otani ?
5. " Kodi ndi wokwatiwa amene'yu ? "
   (i) Mau amenewa analankhula ndani ?
   (ii) Funso limene'li linafunsidwa kwa yani ?
   (iii) Nthawi imeneyi anali kuti wofunsayo ndi wofunsidwayo ?
   (iv) Kodi anali kufunsa za yani ?
   (v) Kodi yankho lache linali lotani (lembani mwachidule).

(vi) Tanthanzani izi pa Chichewa :—

(*a*) Bachelor's Degree, monga B.A.

(*b*) Master's Degree, monga M.A.

(*c*) Doctorate Degree, monga M.D. kaya Ph.D.



Mbumba ya Kalikokha.

A, ndiye Kalikokha.

B, ndiye mkazi wa Kalikokha.

C, D, ndi E ndiwo ana a Kalikokha.

F, ndiye mkazi wa mwana wina wa mamuna wa Kalikokha.

I ndi G akazi adzukulu a Kalikokha.

H, J, K ndiwo adzukulu a Kalikokha.

N, M, L, O, P, ndi Q ndiwo adzukulu-tubzi a Kalikokha.

R ndiye mkazi wa mdzukulu-tubzi wa Kalikokha.

S, T, U, W, X, ndi Y ndiwo adzukulu-thengo a Kalikokha.

Chinthunzi ichi chisonyeza mbumba ya Kalikokha monga m'mene anafunira iye ndiyo D, E, H, J, L, N, Q, U, X, ndi Y. Uku ndiko kulondoloza mbumba modzera mwa Tate, ana ache amuna mpaka zidzukulu zachimuna.

A, ndiye Kalikokha.

B, ndiye mkazi wache.

C, D, ndi F ndiwo ana ache.


E, ndiye mwamuna wa mwana wache.

H, I, ndi J ndiwo adzukulu ache.

G, ndiye mwamuna wa mdzukulu wache.

K, M, ndi N ndiwo adzukulu-tubzi ache.

L ndi O ndiwo amuna adzukulu-tubzi ache.



Mbumba ya Dambudzo.

P, Q, R, S, T, ndi U ndiwo adzukulu-chire ache.

Chitunzichi chisonyeza mbumba ya Dambudzo penanso ya alongo ache aja ndiyo D, H, M, N, P, T, ndi U. Iyi ndiyo mbumba yosalekeza. Koma yodzela kwa ana amuna ingolekeza pa iwo osapitirira ai. Uku ndiko kulondoloza mbumba modzera mwa mai mpaka ana ache akazi mpakanso adzukulu ache onse akazi.

2. *MBUMBA YA KALIKOKHA NDI DAMBUDZO*

Zingalume, Phulantenga ndi Nanthola anali kukula bwino ndithu. Kalikokha, kawiri-kawiri, analikulingalira za ana ache kuti akadayenera kukhala amakhalidwe abwino okula ndi mwambo wabwinonso.

Tsiku lina Kalikokha ana ache atafika pa misinkhu yochenjera, anali kukamba ndi ana'wo namati: "Taonani ana'nu, ine kwathu ndi kutali ku Chingoni kóma a mai anu'wa ndi Achewa. Tsono ndifuna kukudziwitsani kuti inu nonse ana amuna'nu ndinu mbumba yanga yeni-yeni ndipo moyo wanga uli pa inu, koma uyu Nantholo'yu, inde, ndi mwana wanga koma ndidziwa kuti amuna amene adzakwatiwe nao adzamutenga kupita kumene iwo afuna ndipo ana ao ine mwina sadzandisamala kweni-kweni." Bambo uja anapitirira nati: "Ife kwathu ubale weni-weni kapena mbumba yeni-yeni timalondoloza kuchokera kwa bambo ndi kudzera mwa ana ache onse amuna ndi kupitirira kudzera mwa adzukulu amuna okha-okha."

Pamene Kalikokha anali kunena izi, Dambudzo anali pafupi m'khonde mwa nyumba yache ndipo analikumva zonse zimene Kalikokha anali kunena. Atachoka Kalikokha kupita ku mirimo, mkazi wache,

Dambudzo, anaitana ana ache onse nati: " Ana inu ! Ana inu ! Kodi mumanva ana inu ? Tabwerani kuno ! "

Ana aja anapita kwa mai wao ndipo maiyo anayamba kukamba ndi ana ache namati: " Kodi A tate anu aja amati chiani ? Zonse zimene zija musazikhulupirire ai popeza iwo aja amanena zimene zimachitika kwao, ife kuno kuChichewa tiri ndi yathu miyambo yosiyana ndi ya kwao kwa iwo aja. Mverani zimene ndinene ine ndizo zoonadi zoyenera kwathu kuno zimene zakhala zichitika zaka zambiri zapitazi. Inu nonse ndinu ana anga apamtima ndipo nonse'nu ndinu mbumba yanga yokha-yokha. Tere alongo anga aja a Chiipirawachaje ndiwo atsibweni anu ndipo chiri chose chitaonekera m'modzi wa inu, iwo aja ndiwo ali ndi udindo pa inu koma osati Atate anu aja ai, iwo aja adangokuberekani basi. Mukafuna madandaulo, muzipita kwa atsibweni anu ndiponso iwo aja ndiye mwini wache wa inu pamodzi ndi ine ndemwe. Tonse'fe ndife mbumba yao. Icho anganene iwo aja palibe m'modzi akhoza (37) kuphulapo kanthu ngakhale Atate anu (38) sangalandulepo kanthu."

Asanatsirise kumva mau awa, munthu wina dzina lache Tangopitamo (39) amene anali wongopita ndinjira, anamva m'lango ndi mwambo umene mai uja anali kupereka kwa ana ache. Tangopitamo anapatuka, nafika paja panali ana aja nati: " Zoonadi ana inu

muzikonda kumvera m'tsibweni wanu Chiipirawachaje (40) uja kapena Kamkondo ndipo akakhala Atate anu aja adangokubalani kokha basi, alibe mphamvu pa inu ai. Tamverani ndikuuzeni, inu nonse ndinu mbumba ya a Chiipirawachaje ndipo maka-maka ndidziwa kuti mtima wao uli pa uyu Nantholayu popeza mbeu yochokera mwa iyeyu ndiyo idzachulukitse mudzi uno koma iwe Zingalume ndi iwe Phulantenga, mbeu yanu idzalamulidwa ndi alongo ao a akazi anu. Motero kuti mbumba yache ya Chiipirawachaje, irekezera pa inu basi koma ipitirirabe mwa Nanthola mpaka pa ana ache akazi ngakhalenso zidzukulu zache zachikazi." (Pakati pa Achewa mbumba ya munthu imadzera mwa mai mpaka mwa ana ache akazi mpakanso mwa zidzukulu zonse zachikazi. Onani chithunzichi). Zizindikiro zina zoyenera kudziwika tisanalembe chithunzicho :—

A Chitanthauza mwamuna.
O Chitanthauza mkazi.
A Chitanthauza imfa ya mwamuna.
Ø Chitanthauza imfa ya mkazi.
. . . Chitanthauza ukwati wosayenera.
= Chitanthauza ukwati woyenera.

MAFUNSO

1. Fotokozani kusiyana kwa Kalikokha ndi Dambudzo pa malingaliro ao pa za ana awo aja.

2. Lembani chithunzi chosonyeza Kalondoledwe ka mbumba modzera mwa mai mpaka ana ache akazi.
3. Kodi kusiyana kolondola mbumba modzera mwa mai ndi mwa mwamuna n'chiyani ?
4. Nanga izi zitanthauza chiyani ?

   Ø, =, A, A, . . ., O.
5. Kodi Tangopitamo ndani ? Nanga mwambo wache unali wotani ?
6. Lembani matanthauza awiri a mau awa :—

   Adzukulu
   Mtsitsi
   Zingalume
   Ache
   Chire

3. *CHIIPIRAWACHAJE APHUNZITSA MWAMBO WA CHISUWANI*

Bambo Chiipirawachaje ndiye amene anali mwana wachisamba m'banja lija la mai wache wa Dambudzo. Mai wa Dambudzo anali Kuipakuchitakudza ndipo bambo wache anali Nkhondondiananse.

Tsiku lina a Chiipirawachaje anabwera ku banja la Dambudzo atakhuta mowa. Iyeyu atafika, anangoyamba kuzaza nati: " Kodi ana inu atate anu ali kuti ? Ndamva kuti iye'yu afuna kumapingana pingana ndi ine ! Ndamva kuti iye'yu akuti inu'yo ndinu mbumba yache. Kodi iye'yu sadziwa kuti kuno n'kwina, ndiponso iyeyu kwao sikudziwika ? Akabwera, mumuuze kuti ati kuno mwambo wache 'n'chakwanuleka.

" Ngati iye'yu sadziwa ayambe lero, kudziwa kuti ife sitimuwerenga ngati munthu ai, koma tingodziwa kokha kuti ndi munthu wathu wanchito. Tsiku limene ndidzafune kumuchotsa, ndidzamuchotsa ndipo akakhala mlongo wangayu Dambudzo, ndikhoza kukwatitsa kwa amuna ena. Akaonjezanso ndimupanda kochititsa mantha ndithu."

Atatsiriza kuzaza, Chiipirawachaje anayamba kukamba ndi ana aja: " Ana inu, maka-maka iwe Phulantenga ndi iwe Zingalume, osamalingalira zokwatira kutali ai. Ine ndidabereka ana akazi anai ndipo onsewo ndi njole zokha-zokha, moti nonse'nu



Chiipirawachaje apereka mwambo.

mukasankhuleko amene maso anu akadyerere. Ana akazi amene aja ndi asuwani anu ndipo umo ndionera inemo, chikwati cha pachisuweni n'chabwino chifukwa chisungitsa mbeu. Iwenso Nanthola kwathu kuli ana amuna ambiri amene m'modzi wa iwo amene ukam'konde, adzakukwatira. Ine ndalamula, wina osati aphulepo mau ai ! "

Chiipirawachaje anapitirira ndi kuzindikiritsa ana aja za chisuwani: " Ana inu, pamene muona ana akazi a mlongo wa tate wanu, amenewo ndi asuwani anu kapena ana amuna a mlongo wa tate anu amenewo ndi asuwani okha-okha. Koma ana amuna ndi akazi a m'bale wa mkazi wa mai wanu, amenewa ndi abale anu osamasewera nao zina ndi zina za chisuwani ai. Ndiponso ana amuna ndi akazi a m'bale wa tate wanu amene'wa ndi abale anu osamasewera nawo za chisuwani ai. Munthu wosewera za chisuwani ndi iwo amene achitika ngati alongo ache, kapena achimwene ache, amene'yu ndi chitsiru ndi wosamva mwambo."

MAFUNSO

1. Kodi makhalidwe a Chiipirawachaje anali otani ? Nanga mwambo wache kwa mfumakazi zache unali otani ?
2. Pangani ziganizo ndi mau awa kusonyeza kuti mumadziwa matanthauzo ache :—

   Chisuwani, m'bale, mwambo, chisamba, njole.

3. Tanthauzirani izi :—

Kuphula mau, maso adyerera, nkhondondia-nansi, mkamwini ndi wachito, kuipakuchita-kudza, chakwanu-leka, misinkhu yochenjera, kuolobzya miromo, buluzi akhumbira khonde, kupala ubwenzi.

4. *MAKOLO*

Dambudzo kawiri-kawiri anali kuphunzitsa ana ache zina ndi zina zambiri za mwambo wa Chichewa. Nthawi ina anali kuphunzitsa za makolo namati : " Inu ana anga, mvetsetsani ! Ine ndine mai wanu, m'bale wanga wa ine ndi mai wanu wamng'ono kaya ngakhale ndiri ndi abale anga akazi atatu, anai oponda pamutu pangapa, onsewo ndi amai anu ang'ono. Wina atakhalapo amene ine ndidaponda pamutu pache, amene'yo ndi mai wanu wamkulu. Ine ndine mai wanu weni-weni.

Abale a Atate anu'wa ndi atate anu ang'ono pena atate anu akulu koma iwowa ndi Atate anu eni-eni. Alongo ao a iwowa, ndi atate anu akazi ang'ono pena atate anu akazi akulu. Amai ao a atate anu ndi agogo anu akazi a kuchimuna pena akazi anu. Ndipo mai ao a amai anu, ndi agogo anu akuchikazi penanso akazi anu. Koma iwe Nanthola ndi akazi anzako, amene'wa, penanso tikhoza kuwacha asewere ako akuchimuna pena akuchikazi. Koma atate ao a amai ndi atate anu ndi amuna anzanu kapena asewere anu. Koma iwe Nanthola ndi amuna ako amenewa (asuwani). Pokamba nao akazi anu amene'wa, mukhoza kukamba nao zachiphomphwa ndi chinzake palibe kanthu.

Kukula ndi Mwambo

MAFUNSO

1. Chulani matanthauza a mau awa ndipo mupange nao ziganizo :—
   Chiphomphwa, gogo, chinzake, tate wamkazi, asewere.
2. Fotokozani mwambo wa Dambudzo pa za ubale ndi Chisuwani.

5. *KATUNDU APITE KWA YANI?*

Kawiri-kawiri Chiipirawachaje anali kubwera kudzacheza ndi aphwache[53] aja awiri. Zingalume ndi Phulantenga ndiponso mfumakazi[54] yache ija Nanthola.

Chiipirawachaje anayamba kulankhula nati: " Ana inu, inu ndinu aphwanga ndithu, ndipo iyi n'imfumakazi yanga ndithu. Taonani ine ndiri ndi chuma chambiri monga ng'ombe, mbuzi, nkhuku, makasu, mipeni, mitengo ndi zina zotere. Tsono chuma chimenechi ndi cha inu aphwanga. Ine chinthu chitandiona[55], ai, sindidandaula popeza chuma chonse ndiri kukuwerengerani. Pafunika kuti muzidziwa, angadzakulandani anthu adera[56]. Ana anga aja osakawapatsako chuma chimenechi ai, popeza ine simtundu wanga ai. Iwowo ali ndi kwa atsibweni[57] awo kumene ayenera kukatenga chao chuma, ine ukakhala wanga ndi ukwati wokha basi ! Ndiponso ndiri kuuza Amai anu kuti dzina la ufumu limene ndiri naloli mmodzi wa inu ndiye amene adzabvala chidzingwiri[58] chache ndi khoza[59] lache. Ana inu dziwani ndithu kuti ufumu wathu wa ife Achewa, amalowa ndi m'phwako osati mwana wako ai. Nthawi zina amalowa ndi m'bale."

MAFUNSO

1. Kodi malowedwe a ufumu wa Achewa amalowa

ndani ? Nanga chifukwa chache n'chiyani amalowa ndi amene mwachula'yu ?

2. Kodi nanga inu muyesa kuti mwambo wabwino ukadakhala otani pa chuma ? Nanga pa ufumu inu mukadakhala ndi mwambo wakuti azirowa ndani ?
3. Kodi pakati pa mwambo wa Kalikokha, Chiipirawachaje, Tangopitamo, ndi Dambudzo, inu mukadakonda kumvera wa yani ? (Perekani zifukwa zache).

6. *KUPEMBEDZA KWA KALE*

Chiipirawachaje anayamba kulongosola: " Ana inu muyenera kudziwa kuti kudziko kuno kuli mizimu ya makolo athu amene adafa kale. Mizimu imeneyi imabvuta kwambiri ngati sikondweretsedwa ndi zochita zathu. Mwa chifukwa chotero, pamudzi pakhoza kubwera miriri yosiyana-siyana monga nthomba, matenda achirengwa-rengwa ndi ena otere. Nthawi zina pamudzi pakhoza kumajiwa-jiwa anthu pamodzi ndi zoweta zao. Mukadzaona zotere, mudzadziwe kuti azimu aja akufulatirani kotheratu."

Bambo'yo anapitirira ndikulangiza ana aja, " Chinanso chimene muyenera kudziwa, nthawi zina mukhoza kuona kuti mvula sibwera panthawi yache, ichi ndi chirala ndipo gwero lache ndi lomwe lija la kuti azimu sadakondwere ndipo Leza sangakupatseni mvula ai. Chaka chimenecho mukhoza kufa ndi njala ndipo malowedwe a mpupuluzi amakhala omweo. Motero muyenera kuzindikira kuti chirumika chiri chonse, pamene zakumunda zacha, muyenera kupereka mitulo ya zoundukula kwa mizimu. Mukadzaiwala izi, chaka ndi chaka mudzabvutika ndi chirala, azimu atawinduka."

Patapita zaka zambiri, mvula inakanika kubwera ndipo m'mudzi mwa Kambironjo muja munadzala ndi madandaulo ambiri ndipo mfumu Kambironjo

anaganiza zakuti athire mfunde kuti mvula ibwere. M'mawa kutacha anasonkhanitsa anthu ache pabwalo pa nyumba yache nayamba kukamba nao anthu ache. Nthawi imeneyo ana aja anali kumva anthu ali kukambirana popita kukhomo kwa mfumu. Iwowa anali osangalala kuti akaone ndi maso ao zimene Chiipirawachaje anali kuwafotokozera. Onse tsopano anakhala pansi koma anyamata aja anakhala patsogolo peni-peni pafupi ndi a mfumu aja kuti amvetsetse mvemvemve. Mfumu inayamba kulankhula.

Mfumu : " Pepani kuti nonsenu mwabwera pano mwachikhadza-khadza. Koma musaiwala kuti, kaitana kabvula ndipo chiitanitsa nkhwangwa n'chisanu." Anthu onse aja anali ododoma poona mfumu ali ndi nkhope yosasangalala ndipo anachereza makutu ao ndipo sanatsokomola kwambiri.

Mfumu : " Nonsenu mwaona kuti kudziko kuno kwauma, mvula sirikufika. Choterechi n'chija chidaoneka zaka zakale kweni-kweni zija ndipo pakatipa Chiuta, amatipatsa ndithu mvula panthawi yache. Ine zimenezi zandidulitsa mutu wazizwa. Onaninso zoweta pamudzi pano ziri kwangojiwa kawiri-kawiri. Pamudzi pano tsopano palowa mphepo, kodi makhalidwe athu tsopano asokonezeka ? Nanga n'chiyani chirikudzetsa zoopsya zoterezi ? . . . zimene'zi ine ndakhumudwa nazo ! . . . ngati alipo pano anthu amene alikulowa

mmanyumba mwa anzao, kaya kumaba katundu wa eni ache, kaya kusasamala za mwambo wa mdulo otere'wa adzetsa mabvuto ! . . . Amene'wa aumitsa dziko ! . . . azimu atifulatira ife ! Kodi Mphambe, Chiuta, Leza akhoza kutipatsa mvula ife ? "

Anthu onse aja anachita mantha ndipo anagwetsa nkhope zao pansi, ena anayamba kugwetsa m'sozi pansi ndithu. Mau amenewa anawalasa kumitima.

Mfumu : " Tsopano lino nonse'nu pitani kunyumba kwanu, phikani mowa, konzani ufa ndi zina zotere kuti tikapereke mitulo kwa azimu kuti atipemphere mvula kwa Leza wathu, Mphambe yathu ndi Chisumphi wathu amene wakhala natisunphirira ndi kutiutirira pa zaka zonsezi. Amene anali kuyenda kuipa tsopano aleke ! . . ."

Anthu onse anabalalika, nayamba kukonzekera za kukapereka nsembe yokaitanira mvula. Monga unali mwambo wache, mlongo wamfumu ndiye amene anali pa chinchito chokonzekera zonse zatsikulo kuti mvula ikabweredi. Ena ache achangu, anayambiziratu kumakapereka tinsembe tao kutinyumba ta azimu amakolo ao. tizinyumbato timachedwa tiakachisi. Bere liri lonse la banja linali ndi timakachisi toperekeramo tinsembe tao kwa mizimu yamakolo awo. Mudzi uja unali gwede-gwede kukonzekera tsiku lalikululo.

Masiku atakwana, mfumu ija inatumiza mau

kunyumba iriyonse kuti usiku wakuti mawa kulikupereka nsembe, m'mbanja monse anthu ayenera kugona payekha-payekha. Anthu onse anamvera mau a mfumu nachita monga adachenjezedwa. M'mawa kutacha, mfumu analawirira kumtengo wothirirako mfunde (woperekerako nsembe) uja kuti akakambe ndi azimu anthu onse asanabwere. Atafika anayamba kulankhula.

Mfumu : " Zikomo ! . . . Zikomo ! . . .
Tifikakotu uko ! . . .
Ichotu . . . ichotu ! . . .
Zikomotu . . . ! "

Nthawi imeneyi anali kuyenda monyakaika osachita mgugu ai. Thupi lache lonse anali atalikhumatitsa kusonyeza ulemu, nafika patsinde pa chimtengo chachikulu chobvwandamuka chokhala ndi akalungusese ambiri-mbiri, kamdima-dima kali kwani-i-i, nkhandze yochita chobzyala iri, ndi-ndi-ndi, kaulemerero-lemero kali gu-u-u-u.

Mfumu tsopano inayamba kulankhula ndi azimu (amanda), ngakhale sanali kuwaona koma anali ndi chikhulupiriro kuti azimu anali kumva.

Mfumu : " Pepani ndithu ife ana anu tiri kubwera madzulo ano kudzakupembedzani, kudzakupatsani nsembe kuti mutipatse mvula. Tiri kudzapempha mvula ndiye musayendere kutali ndithu. Mutimvere ife ana anu."

Atatha kulankhula, a mfumu anapita kumudzi

kukadziwitsa anthu za nthawi yokapemphera mvula. Dzuwa litapendeka, azirongo ache onse a mfumu anasenza phala ena ufa ndipo anthu onse ena aja anali kutsatira kupita pamalo aja. Atafika pafupi mfumu anaodira.

Mfumu : " Zikomo ! Zikomo ! . . .
Tabweratu ife tsopano . . . !
Zikomotu . . . Zikomo . . . ! "

Mfumu inauza anthu aja kuti afike kufupi mwaulemu.

Mfumu : " Nonsenu tsopano khalani pansi mwaulemu, mafumu enanu khalani apo, azimai'nu khalani apo, iwe mlongo wanga wamkulu Mdambizana khala pafupi ndi ine. Nonsenu khalani chete tsopano."

Anthu onse aja maso ao anachita kuti yu-u-u-u-u, pa mfumu ija ndi mlongo wache uja Mdambizana. Tsopano Mdambizana anayamba kulira mochula maina a makolo ache onse motere :—

Mdambizana : " Mayo ine ! tiri mmabvuto ife kuno iwe Chatepera-a-a-a-a ! Nditani ine iwe bambo Sonkhwe-e-e-e ! Mvula yakanika nanga ife tiione kuti ? Pepani msatiumire mtima ife ana anu kuno-o-o ! "

Mfumu : " Mamawe-e-e-e . . . hi-hi-hi !
Bambo Mtekanjiru iwe-e-e-e !
Mai Mdauyana iwe-e-e-e-e-e !



Mafumu ndi anthu apempha mvula kwa azimu.

Ayo ine-e-e-e-e . . . hi-hi-hi !
Kum'mero kwauma ife-e-e-e !
Tikufa ndi njala mayo-o-o !
Mudatisiyira nkhondo mayo-o-o !
Tidalakwanji Kalanga ine-e-e-e !
Mayo ine-e-e-e-e-e ! Mayo ine-e-e-e-e !
Ndiwalera bwanji ana mayo-o-o-o !
Ndiusunga bwanji mudzi mayo-o-o-o !
Tipatseni mvula nditani ine-e-e-e !
Inu Chiuta mvula tipatseni-i-i-i-i !
Inu Leza madzi mutipatse-e-e-e !
Inu Chisumphi tidalakwanjiye-e-e !
Inu Namalenga tidyanji ife-e-e-e !
Gogo Chirumpha m'datisiya ife-e-e !
Tazunzika nao umasiye ife-e-e-e-e !
Nditani ine, nditani ine-e-e-e-e-e !
Pakhala chirombo, chikadangopha ine-e-e !
Imfa tenge, tenge, tenge ine-e-e-e !
Taonani anthu'wa ndiwatani ine-e-e !
Kalanga toto ! Kalanga ine-e-e-e-e-e !
Tipatseni mvula, tipatseni lero-o-o-o !
Ngakhale mochepa landirani izi-i-i-i-i !
Landirani Mphambe, landirani tsono-o-o-o !
Mvula bwerani ! Mvula bweretsani-i-i-i!
Tibvumbweni tonse kummero kwauma-a-a-a ! "

Nthawi imeneyi anthu onse aja anali mitu zvoli-zvoli ndi chisoni chifukwa chakudandaula kwa mfumu. Ena pakhosi panangochita ngati patseka chinthu ndipo ambiri maso ao anali odzaza ndi misozi, ena mizosi inalikutsika ndithu mmasaya. Nanga inu owerenga za mbiri imeneyi simulikumva chisoni kodi? Mfumu anapitirira ndikulankhula.

Mfumu: "Ife tabwera tikuti mutipatse mvula chifukwa kudziko kuno kwauma, ife ana anu tingafe ndi njala."

Tsopano mfumu anatembenukira mlongo wache namuuza kuti ayambe kuthira mowa pang'ono m'kambiya ka azimu. Tsopano anayamba kuthira ufa pang'ono, ndi zonse zimene anabwera nazo, anathiramo pang'ono-pang'ono. Kambiya ka azimu kaja kanali patsinde pa mtengo paja. Nthawi yomweyo onse anayamba kubvina mosangalala, ena kumathirana ufa, ena kumawazana mowa, ena kumachita ngati kugwirana, ena kumachita ngati masewera opandana, ngati chipaka ndiponso kumachita ngati kupirikitsana. Nthawi imeneyi anali kuyimba nyimbo zambiri ali kumachita ngati ali kubwerera kumudzi kwao kuja.

Panthawi imene anali kuyimba nyimbo'zo, panalibenso zoopana kuti awa ndi apongozi, kaya uyu ndi mkamwini, kaya uyu ndi mwana wanga ai, inali nthawi yachipembedzo. Nyimbo zimene anali

kuyimba m'manja muli kutibuka nchembere ziri kuting'uka zinali zotere:

1. *Kolole*

Mtsogoleri: Mvula Kolole mvula !
Onse: Kolole !

2. *Kantambo*

Mtsogoleri: Kamtambo ndi aka ndi aka ! *DC.*
Onse: Kanya mvula ndi aka Kamtambo !

3. *Siyo Mvula*

Mtsogoleri: Siyo mvula-a-a-a-a-a-a-a ! *DC.*
Onse: Kumsinja yafika-a-a-a-a-a !

4. *Msamakana*

Mtsogoleri: M'samakana, m'samaka
M'samakana, m'samakana-a-a-a !
Onse: Mvula ikananso-o-o-o-o-o-o-o !

5. *Pam'tum'tupo*

Mtsogoleri: Foleranl nyumbayo-o-o-o ! *DC.*
Taonani myula yafika-a-a !
Onse: Pam'tum'tupo-o-o-o-o !

6. *Mereraye*

Mtsogoleri: Madzi apamwalaye-e-e-e ! (Kawiri)
Onse: Mereraye-e-e-e-e !
Mtsogoleri: Waiona ndaniye-e-e-e-e ?

Onse : Mereraye-e-e-e-e !
Mtsogoleri : Nanga a Kalum'bu kwao-o-o-o !
Onse : Mereraye-e-e-e !
Mtsogoleri : Yede-yede-yede-yede
Nanga-nanga-nanga
Omati n'tani-i-i-i !
Onse : Mereraye-e-e-e-e-e !

7. *Mvula*

Mtsogoleri : Mvula-a-a-a-a ! *DC.*
Onse : Kolole-e-e-e !

8. *Gokwe*

Mtsogoleri : Mvula-a-a-a ! (Kubwereza kanai)
Onse : Kolole-e-e-e-e !
Mtsogoleri : Kamtambo ndi aka ndi aka-a-a-a ! (Kawiri)
Onse : Kanya mvula nd'yaka Kamtambo-o-o-o-o ! (Kawiri)
Mtsogoleri : Gokwe-e-e-e ! (Kawiri)
Onse : Kolole-e-e-e-e-e-e-e !

9. *Tipatseni Madzi*

Mtsogoleri : Mvula ! mvula-a-a-a ! (Kawiri)
Onse : Kolole-e-e-e-e !
Mtsogoleri : Tipatseni madzi (Kawiri)
Kummero kwauma-a-a-a-a !
Onse : Kolole-e-e-e-e-e-e-e-e !

10. *Namalowe*

Mtsogoleri : Namalowe ! Namalowe-e-e-e-e !
Onse : Mvula n'dzenayo-o-o-o-o-o-o !
(Kumangobwereza)

11. *Kwathu Kuno*

Mtsogoleri : Mvula ko-ko-ko
Mvulaye-e-e-e !
Onse : Kolole-e-e-e-e !
Mtsogoleri : Kwathu kuno (Kawiri)
Kwa Khuthe,
Ndiko umabvumbwa-a-a-a-a-a !
Onse : Kolole-e-e-e-e-e-e-e-e-e !

12. *Kumchenga*

Mtsogoleri : Mvula-a-a-a-a (Kawiri)
Onse : Kolole-e-e-e-e !
Mtsogoleri : Tungani madzi (Kawiri)
Kumchenga kwauma-a-a-a !
Onse : Kolole-e-e-e-e !

13. *Zimatere*

Mtsogoleri : Zimatere-e, Zimatere-e-e-e !
Onse : Bwenzi zikoma-a-a-a-a !
(Kumangobwereza)

Anthu onse aja tsopano anali kuthamangira kumudzi nyimbo ziri pakamwa. Asanafike kumudzi, anaona



Mafumu ndi anthu athawa mvuta.

mtambo wamvula mbali ya kunyanja. Anthu aja poona mtambowo, anakangaza kuyimba ndipo posachedwa chimvula chamatalala chinagwa, anthu anakafika kumudzi ndi mvula ndipo anabvumbwa koopsya. Atalowa m'manyumba, anayamba kumwa mowa wao uja mosangalala ndipo dziko lonse linatama mfumu Kambironjo chifukwa cha mapemphero ache a mvula olula.

Mfumu ija inali ndi njira zambiri zopempherera mvula. Nthawi zina ankatenga ana akazi ang'ono-ang'ono, maka-maka adzukulu achisamba, mwina mwana wache wamkazi, napita nao kukachisi atatenga mowa, magazi ang'ombe, ndi nyama yache. Atafika pakachisi uja anali kupemphera chotere :—

Mfumu : " Tipatseni mvula !
Tichitireni chifundo."

Tsopano natenga fodya naika mkachisi muja, m'meneno alikuchula maina a anthu amene adafa kale. Natenganso mowa nathira pa m'kambiya kaja, nayamba kupempheranso kwa azimu.

Mfumu : " Tithandizeni, tabvutika ife ana anu, mwatiumira mtima."

Natenga nyama ija naika mukambiya muja, nalankhula, " Pepani ndithu mutichitire ife chifundo." Nthawi imeneyi anali atabvala nsalu zakuda, nayamba kuyimba ndi kumabvina ngati zija tachula kalezi.

Nthawi yakuti zakumunda zabereka bwino ndipo kuti zacha, ankatenga zoundukula n'kumakapereka kumakachisi ao aja kuti ayambe kudya, ndi azimu kuti akondwere.

Mvula ija ikamangodzera-dzerabe, akulu-akulu ankapangana kupita kumene adathirira mfunde atabvala zoyera napita pakachisi uja nang'amba tsindwi, posakhalitsa kunkachita ng'amba kunja, mvula osagwanso chifukwa patsindwi pa kachisi panali pong'ambika. Iri ndi gwero lache la ng'amba. Mfundezi zinali kuthiridwa kapena pa tsinde lamtengo, pena pakachisi wapatsinde lamtengo wobvungumala, pena padziwe lalikulu (mwina pafupi pache ankanjatanso kachisi wamizimu'yo). Nthawi zina pamene mtsogoleri ali kupemphera, namachula

maina a anthu akale mmenemo ali kupereka nsembe zija, anthu onse oonerera ankabvomera moomba m'manja namanena kuti, " Pepa-a-a-a ! "

Nthawi zina matenda akakula pa mudzi, onse apabanjapo ankapangana kukapereka nsembe ku tiakachisi tao. Mwina mfumu ikaona kuti mliri wakula m'mudzi mwache, inkapangana ndi alongo ache aja pamodzi ndi akula-akula ena kukapereka nsembe kukachisi ndipo mapemphere ao onse ankamveka. Kawiri-kawiri, akaona zododometsa ankapita kwa wa maula. Uja woombeza ndiye anali kuwadziwitsa kuti ayenera kupereka nsembe chifukwa mizimu ya ambuye wao amene adafa kale iri yosakondwa.

MAFUNSO

1. Lembani mosapyola mau 400 za mapemphero amvula akale.
2. Chiipirawachaje anaphunzitsa zotani za mfunde ?
3. Lembani pemphero la Kambironjo la mvula la patsinde pa mtengo paja.
4. Lembani nyimbo ziwiri za mfunde za izi :— Mereraye, Kwathu kuno, ndi Gokwe.
5. (*a*) Kudziko kwauma, mvula sirikubwera ndipo inu ndinu mfumu yosunga mudzi. Lembani chimangiriro cha pemphero la mvula limene inu mukadachita pokathira mfunde.

(*b*) Kodi nanga atakhala masiku ano mukadachita chiyani ?

6. Lembani ziganizo ndi mau awa kusonyeza kuti mudziwa matanthauzo ache :—Mfunde, lula, azimu (amanda), kachisi, zoundukula, kubvungumala, mvula, chipembedzo, mliri, chirala.

7. *CHOKOLO*

Chiipirawachaje anapitirira ndi kulanga ana mwambo nati: " Iwe Zingalume ndi Phulantenga, muli kuchitaku n'kukula ; ndipo pafunika kuti muzidziwiratu zina ndi zina. Misinkhu yanuyi yakula-kula ndithu ndipo malingiiriro anu azi-yamba kukhwima koposa. Muyenera kuzindikira kuti m'tsogolomo wina wa inu atasowa, amene adzatsale afunika kudzakwatira mkazi wofedwayo kuti asungidwe bwino Uku timacha kulowa chokolo.

Kawiri-kawiri pa nthawi ya maliroyo, mkazi wofedwa amakonda kulira koposa ndithu. Polira mkazi amakonda kuchula mau ambiri omvetsa chisoni." Chiipirawachaje anapitirira nati, " Inu muzikalira monga mom'sangalatsa motere : Kazi-rira nupenya ine, kazirira nupenya ine." Ana aja anati, " Kodi zimenezi zidzaoneka liti ? " Iye anati, " Mtsogolo, ndipo mwinanso sizingachitikenso n'komwe koma kungofuna kuti muzidziwiratu zinthu zozama za akulu-akulu athu oyamba."


8. *MWAMBO WA NCHITO ZA PA BANJA NDI MWAMBO WOYENERA MUNTHU WOKHWIMA MSINKHU*

Nthawi imeneyi ku nyumba ya Kalikokha ndi Dambudzo kunabadwa mapasa akazi okha-okha, Mwasanya ndi M'meendo. Patapita nthawi, wina wa mkazinso anabadwa dzina lache Mpokosa.

Kawiri-kawiri Kamkondo ndi Chiipirawachaje anali kulankhula ndi ana a mlongo wao uja Da-mbudzo, kuwasonjeza zimene ayenera kukonzekeratu asanalowe m'mabanja ao.

Kamkondo anali munthu waluso losoka mphasa koma Chiipira anali waluso losema ndipo Dambudzo, mai wao, anali waluso la zoumba monga mbiya ndi zina zotere.

Kamkondo tsiku lina anati : " Ana inu, muyenera kumatulukira-tulukira pamabwalo pamene akulu akusokera zitete. Motere, mukhoza kutola nzeru, ndipo simudzaoneka anthu opusa mtsogolo pamene mudzapita pa mudzi wa eni pa nthawi ya ukwati ndiponso mudzakhala ana osachititsa manyazi popeza sipadzaoneka chokulakani. Nthawi zonse ndimanena ine kuti mwana wosadziwa zinchito ndi chitsiru ndipo anzache adzamuseka nthawi zonse."



Kamkondo aphunzitsa nchito zamanja.


Chiipirawachaja anati: " Ana inu mukhale ana akumva kamodzi, nonsenu kupatula alongo anu, muyeneradi kudziwa maluso ambiri monganso zosemazi. Mwana wosadziwa nchito atukwanitsa atsibweni pamodzi ndi mafumu. Anthu sali bwino ndi chipongwe masiku ano, ndiye nthawi zonse muzibwera ku nkhalangoku kumene tidagwetsa mitengo yosema mitondo ndi zipande kuti muziphunzira. Ine ndifuma ana ochotsetsa manyazi."

Zingalume ndi Phulantenga, analimbikira koposa kuphunzira nchito zamitundu-mitundu. Nchito zina anazipindula ndizo :—kusema mipini, kuluka nsengwa ndi zitete, kusoka mphasa, kusema mitondo, mithiko, zipande, mauta ndi zina zotere.

Dambudzo anati: " Iwe Nanthola, nthawi zonse uzionera m'mene ndichitira inemu ndipo makamaka uyenera kusamala kuphunzira m'mene ine ndimaphikira chakudya, m'mene ine ndimafululira mowa, ndiponso m'mene ine ndimaumbira mbiya. Ngati udziwa nchito zimenezi, udzakahala mkazi wochititsa chidwi ndipo amuna ambiri adzakukhumbira." Nanthola anadziwanso zinchito zambiri zina monga kulocha nyumba, kulocha mbiya ndi zina monga zachulidwa kale.

Zingalume ndi Phulantenga anaphunzira zina Zambirinso.

Kalikokha anaphunzitsa ana aja magule ena otere :



Nchito zamanja zimene anyamata anaphunzira.

Mwambo wa Nchito za Pa Banja Ndi Munthu Wokhwima

Mitundu ya magule :


Khunju	Kansengwa, Chimtsita
Gulutu	Chiterera
Kacheche	Masalimo
Nteketa	Chitoto
Chamba/Kazukuta	Kanonomera
Mdanganya	Nkhuwiri
Sisiri	Mjiri
Gonje	Chisamba
Gwetsa	Kasodo
	Chikwapu
	Kapala

---

1. Mphasa. 2. Chipanda cha mowa (Kajodola). 3. Chipanda cha mowa (Kandunde). 4. Chikho cha mowa (mkobwe). 5. Mbale yamtengo (ndiro, ngwembe). 6. Chipanda cha mowa (mbwafu). 7. Chipanda Chamafuta (nsupa). 8. Chophikira cha mtengo (mthiko). 9. Chipanda choning'a chachikulu (guda). 10. Nsengwa Zosakunga. 11. Nkhwangwa. 12. Munsi (Mnsinjo). 13. Mtondo. 14. Uta. 15. Mpaliro. 16. Ngombe. 17. Chipande. Magawo a mpaliro :—18. nthera ; 19. kauli ; 20. bano ; 21. Chiridzo (Chamtengo Chamkati) ; 22. Mubvi. Magawo auto :—23. nsinga ; 24. ngolowodza ; 25. pamimba (mimba ya uta) ; 26. nsala. 27. Mosungira mipaliro : phodo.



Dambudzo aphunzitsa nchito zamanja.



Maluso ena amene atsikana anaphunzira.

Kalikokha anaphunzitsanso ana ache za magule ena amene anakayaona ku maiko a kumwera kwa dziko la Malawi monga awa :—

Siribu, njipi, chitsukulumwe, nyakwale, pango, mtseke, phitimbi, katego, tosa, tandaliko, chikwizire, chibuli, utse, beni, maseseto, lundu, mabzyoka, fukula, gaka, malambo, likhubwa, theula, kapolombe, bangwe, mfintha, nakwale, chipinde, nkonde, chiponda, chisakasa.

Ana a Kalikokha anali odwabwitsa chifukwa anadziwa kubvina magule ambiri akale.

Kalikokha anaphunzitsanso zoimba-imba za mitundu iyi :—

Nsansi, kaligo, limba, mkangala, bangwe, lingaka,

toliro, zeze, ng'oma monga mpanje, nthipi, mbalule, mseche, ndewere, gunda ndi zina zotere.

Zoimba-imba zina zinali izi :—Magologodo, mphalasa, maseche (mtseche) ndi mangwere.

Kalikokha anali munthu wa luso pa zoimba-imba ndipo anagawa magulu a zoimba-imba zonse motere :—

Gulu loyamba. Za mtundu wazokhala ndi Zingwe.

Bangwe, mkangala, kaligo, zeze.

Gulu lachiwiri. Zamtundu wazokhala ndi Chikopa.

Ng'oma za gule wamkulu, monga : ndewere, Mtiwiso, mbanda-mbanda kayanso nthipi.

Gulu lachitatu. Za mtundu wa zouzira mphweya.

toliro, poliro, mbètete, mphalasa, lingaka.

Gulu lachinai. Za mtundu wa zogogoda, wa zowayasa, ndi zakhodola.

Magologodo, nkhwende, mngwiri/mliu, njiwiri, maseche, limba, nsansi.

Kalikokha anaphunzitsanso ana ache za mitundu ya misampha monga iyi :—

Mono	= msampha wa nsomba.
Goba	= msampha wa mbewa pena nchenzi.
Khukhulule, Khwekhwe	= Msampha wa mbalame zouluka ndi za mminda.
Ukonde	= msampha wa nyama za m'chire, wachingwe.
Mbuna	= msampha wokumba dzenje wa nyama.

Ulimbo	= msampha womata mbalame.
Khoka	= msampha wachingwe, wophera nsomba.
Mbedza	= msampha wokolera nsomba.
Kombe	= msampha wophera mbalame usiku.
Golo-golo	= msampha wophera mākoswe.
Diwa	= msampha wa mwala wophera mbewa.

Dambudzo anapitirira kuphunzitsa ana ache akazi za zina zowathandiza kuti akhale ndi maonekedwe okongola ndipo anati: "Nanthola, ndi ana inu nonse kuti mukhale okongola pafunika kuti muteme mphini, kumaso, zam'litsipami ndiponso osaiwala chitopole pa mphumi ndicho chimene amakonda kufera ana amuna chimenecho. Chofunika chinanso, ndi m'chome m'masayamu, ndipo pamitu panupa pafunika kuti zichechi ziwiri zisamamerera tsitsi. Mduliro ndicho chinthu chachikulunso chimene sichiyenera kuiwalika. Mphuno yakumanzere'yi ifunika kuidoola kuti muziikapo chipini cha mtengo waphingo ndiponso mano anu afunika kuwanga kuti akhale ali ndendende. Mudzaona kuti poseka, mudzaoneka okongola koposa. Makuta anu afunika kudoola kuti muziikako pherere la mtengo uli wonse (ena amati ndolole kaya nsapule)."

Dambudzo anapitirira ndi kunena kuti, "Ana inu, simuyenera kuiwala kutemanso mphini mu aka-tumba'mu, m'nchafu'mu, pa mimba'pa ndiponso pa

mtima'pa, maka-maka pakati pa maerepa ndipo chitopole pamene'pa chimakhala bwinonso. Chinanso pafunika kuti m'khosi muzibvala mkanda wambiri maka-maka wamtambo, wakashuga ndi wachikasu. M'manja ndi m'miyendo pafunika kubvalanso mkanda umene amaucha zinchoto kapena chiona-alongo, Kawiri-kawiri mudzaoneka okogola kuposa akazi onse ngati mutamabvalanso chikono, makoza ndi mafumba. Mafuta amene akhoza kukuonetsani maonekedwe abwino ndi ansatsi amene ayenera kusungwidwa bwino mu nsupa Msupamo pafunika kumaikamo nsanza zakuti zizisunga mafutawo."

Dambudzo anapitiriranso ndi kunena mwachidule motere : " Ana inu ndinaiwala kukuuzani zina ndi zina zoonjezera pa zija ndanena kalezi. Mphini zija za mlitsipazi dzina lache timati *nkonde*, ndipo m'masaya'mu timatema zina dzina lache mapazi-a-njiwa, zina zichedwa *kanjedza* (maonekedwe ache). Zina zache ndi za mmisana'mu mpaka m'matako'mu dzina lache timati **Chithyolaulendo* kapena *chiphwa-nyaulendo*. Za m'chafu zonse timacha kuti *matipa*, za m'nthanthula'mu timazicha kuti *chiona-ankhoswe* ndipo za m'mikono'mu timazicha kuti *kapereke-nsima*. Zinanso za pamimba zozungulira mchombo zichedwa *chivangata-mchombo*. Zobvala zamakolo athu onani izi ankaomba ndi bwazi dzina lache ndi *chiondo* kapena *dewere*. Onaninso zochokera m'khungwa

la mtengo zinali izi :—nkhwindi, ndondo, njicha, chibaphi, m'manga-nyama, senzi, *chimbwi*, *nkhwende*, *njereka*, *chidawa*, ndi chimodzi-modzi ndi *m'manga-nyama*, zonsezi muyenera kumazidziwa." Dambudzo anali kukamba mofulumira. Ife tsopano tirongosola momveka bwino, motere :—

Zobvala zakale : (za Azimai).

Chibaphi	= Chobvala cha mkati.
Njicha	= Chobvala cha pamwamba pa Chibaphi.
Ndondo	= Chobvala pamwamba pa njicha.
Nkhwindi	= Chobvala pamwamba pa Ndondo.
Chimbwi	= Nsalu ya thonje.
Nkhwende Nyanda	= Nsalu ya khungwa la mtengo.
M'manganyama	= Chobvala chakhungwa la mtengo, chobvala mkazi wapakati.
Chidawa	= Chobvala chakhungwa la mtengo, chobvala mkazi wapakati.
Senzi Ngayo Chitsimpho	= Chobvala cha akazi chonjata maere (ngati kamisolo).
Njereka	= Chobvala cha azimani kumaso ndi kumbuyo, mtundu wa njicha, nkhwindi ndi zina zija.

Zobvala zakala (*Amuna*).

Nguwo = Chikopa chofufuta.
Thewera = Chobvala cha khungwa. la mtengo.
Mwado = Chobvala amuna chopangidwa ndi ntibo wa chikho, kubisa maliseche! (Izi zinadza ndi Angoni.)

Mawerengedwe Akale

Dambudzo anaphunzitsa ana ache mawerengedwe ochedwa "kamba," otere :—

1. Kamba wadwala.
2. Wadwalanji?
3. Wadwala mutu.
4. Mutu umene.
5. Udadza ndiyani.
6. Udadza ndi nsira.
7. Nsira amene.
8. Kamuitaneni.
9. Tidzamuombeze.
10. Gumba wagumbala.

Dambudzo anaphunsitsanso kuwerenga kwina kochedwa *Tekiteka* motere :—

1. Teki.
2. Terera.
3. Teka.
4. Masamba.

5. Mvirombiro.
6. Kumuluma.
7. Changali.
8. Chalira.
9. Sitoli.
10. Sinkumi.

Dambudzo anapitirirabe ndi kuphunzitsa ana aja nati, "Ana inu, muchitaku n'kukhwima ndithu, ndipo popeza mwayamba kumera maere, pafunika ndikuphunzitseni mabvalidwe oyenera maka-maka iwe Nanthola, kwaya mpango uwu wa nsalu yabiriwita uzinjata m'chifuwamu kuti maerewa azibisika, ndipo wina suwu mkwamba wa usanza uonjezere m'chiuno'mu kuti uzibvala mwaumunthu ndithu, popeza nsalu yogauka-gauka poyenda ichotsa ulemu wa munthu."

Nthawi zina Dambudzo anaona kuti akadayenera kudziwitsa mwana wache uja Nanthola za zina za mankhwala othandiza pa miyoyo yachikazi ndipo anati, "Mwana iwe, chinanso choyenera kuti uchidziwe ndi mankhwala a 'konda ine.' Mankhwala amene'wa amathandiza kuti amuna azikhoza kukukonda. Upite kuchire ukakumbe muzu wa mtengo wa mlirira, muzu wa mpetu, ndi muzu wa mwanano ; ndipo ukafunenso chisa cha soniho ndi chitenkhwa cha ng'ona ndiponso ukakumbe muzu wa palibekanthu." Zonsezi pafunika

kuzitentha ndi kukala mkala ndipo pafunika kutemera mkalawo m'psyakapsyaka mwa zala zakumanja ndi miyendo ndiponso pa mphumi. Monsemo ufunika ndi muwadzo umodzi-umodzi. Amuna onse azidzangosonthokera iwe, kulirira iwe, kupetukira kwa iwe, kuyanjana ndi iwe ndipo ambiri azidzangoti, palibe kanthu, ameneyu ndimukwatira. Chotsiriza pafunika kusungunula dothi lina lochedwa chiumi m'madzi ndi kumasamba madzi ache. Amuna adzakuumirira nthawi zonse."

Dambudzo anapitiriranso ndi kulangiza Nanthola za makhwala ena ofuyira mwamuna kuti asamakonda akazi ena koma iye yekha, nati, " Nanthola, mwina mtsogolo udzapeza banja ndipo uchenjereretu kuti akazi ena angadzakulande mwamuna. Pafunika kuti iwe udziwiretu mankhwala ofuyira mwamuna. Pafunika kupeza muzu wa nsakadzinja, muzu wa mleza, mchira wa thunga (buluzi), chisa cha katawa ndi chisudzu. Izi zonse ziyenera kumangidwa m'khoko la chimanga ndi kutentha ndi kukala mkala wosokoneza ndi mchere kuti zioneke ngati khundabwi. Kawiri-kawiri pafunika kumafutira m'ndio zonse. Pochita izi udzaona kuti amuna ena adzasudzula akazi ao ndikufuna kuti akwatire iwe, malinga ngati wotero'yo utamudyetsa ndio zakozo, ndipo kawiri-kawiri amuna ako sadzakhala oyenda-yenda ai."

Kalikokha anasonkhanitsa ana ache amuna nati,

" Ana inu, tsopano mwafika pa msinkhu waunyamata ndithu, ndipo muyenera kudziwa zina zambiri monga za mankhwala. Poyamba mudziwe mankhwala a mfumba kuti mtsogolo njala ingadzakubvuteni. Pofuna izi, muzitenga fukutu, chimpsyimpsyi cha ba msika, makoko a pamphambano, dzira losukusa, chimbalu cha mtondo ndi dothi lapadiwa, zonse kuzikulunga m'nsalu yapadzala ndi kutaya kunkhokwe maso ali otsinzina. Patapita masiku ena pa nthawi yomera m'mera, pafunika kutenga phukusi la mankhwalalo ndi kumayenda nalo m'minda ya ena ndi kumanena mau awa :—

Mkupa, mkupa,
Tiye muno, tiye muno,
Kafumbu, kafumbu,
Tsala muno, tsala muno.

" Poyimba nyimbo imeneyi, mudzaona kuti pokolola mudzapeza chimanga chambiri m'munda mwanu."

Ana aja anali okondwa kwambiri popeza njira yachidule yopezera chimanga chambiri.

Kalikokha anapitirira ndi kufotokozera ana ache za mankhwala amitundu-mitundu ndi machitidwa ache motere :—

Mangolomera (*Mphamvu*)

Pfupa la Njobvu.
Madzi a m'nkhali.

Nsakadzinja, muzu wache.
Bololo.
Dothi la pachulu.
Dothi la pachiumdo, ndi
Chipala chapamoto.

Machitidwe ache : Zonsezi zifunika kutentha ndi kumatemera m'manja ndi m'miyendo.

Mtsiriko

Muzu wa Bwandama.
Mitengo ya Nkhwichi.
Gonondo.
Swiswiri ndi
Mfundo ya bango lapadziwe.

Machitidwe ache : Kugawa pawiri ena kutentha ndi kumazirira m'nyumba koma ena afunika kumathira m'maenje a nsichi pa nthawi yomanga nyumba. Izi, zichitike ndi mtsibweni wa m'nyamatayo.

Kalikokha anati: " Mankhwala awa athandiza kutsirika nyumba kuti mfiti isalodze anthu m'nyumbamo.

Muzu wa Nthungwi.
Ching'aning'ani.
Galang'ande.
Mutu wa kadzidzi.
Mapiko a namzeze,
Maso a fisi, ndi mphuno za galu.

Machitidwe ache : Zonse zitenthedwe ndiponso zikalidwe ndipo gawo lina athire m'madzi, ena ndikumasamba m'maso, ena afunika kutemera pamphumi."

M'dulo

Chidulo cha m'chichezo chakale,
Chidutswa cha mphasa zakale,
Dothi la chiumi,
Madzi a panolo,
Dothi la pa bwalo la gule, ndi muzu wa mlungalunga.

Machitidwe ache : Zonse kutentha ziri zosanganiza ndi mchere ndikumadya monga khundabwi. Nthawi zina kumathira m'ndio.

Liombo

Chapuzi,
Chipalanyenje.
Dinde,
Mbadi ya Chiboli,
Mpoza.

Machitidwe ache : Onsewa afunika kusansantha ndi kuumba nchinchi. Zitatha kukonzeka izi, pafunika kuika pa liombo la mwana kuti mutu ungagawanike pawiri.

Chironda

Mbvuunguti,
Mpoza.

Machitidwe ache : Zonsezi kuzisinja ndi kumamata pa chironda kaya kumafinyira pachironda madzi achewo.

Thupi

Mphambano,
Chitenkhwa cha ng'ona,
Mchira wa Fisi.

Machitidwe ache: Zonse kuzisokera m'njirisi ndi kumanjata padzanja lakumanzere pena m'chiumo. Kalikokha anati, " Mankhwala amenewa athandiza kuchinjiriza nao ku machenjerero a mfiti kotero kuti sizingathe kudzakutambirani ai.

Litsipa (*Loyamba*)

Muzu wa Kangaluche.
Kanyanyame (kanyaminyami)
Muzu wa tsabola ndi mwavi wakutsindwi.

Machitidwe ache : Kuzipera zonse ndi kumatemera m'litsipa miwadzo iwiri-iwiri.

Litsipa (*achiwiri*)

Mlumiko.

Machitidwe : Kutenga liphondo la nyanga ya insa ndi kulumika m'litsipa. Mtsempha wa litsipa ufunika kuudula kuti chimene chiwawacho chituluke pamodzi ndi mwaziwo.

M'mimba

Muzu wa likodza, makungwa a naphini,
Muzu wa Mlusu.

Machitidwe : Kubviika m'madzi ndi kumamwa madzi ache.

Obera/Mgoneko

Mchira wa Fisi.
Mphuno za fisi, ndi
Kadyaligona.

Machitidwe : Zonsezi kuzinjata mtolo umodzi ndi kumayenda nao. Anthu adzagona tulo tofa nato.

Kuombeza

Mkhate wa madzi amankhwala.
Nthenga ya Mphungu pena Nthiwatiwa.
Nsupa zomezana.

Machitidwe : Izi zithandiza kugwira mfiti kapena kuona amene adachita chiwembu. Machitidwe ache tifotokoza kutsogoloku.

Ulimbo

Mtengo wa Mpetu,
Nsomphole.

Machitidwe : Kupala zonsezi, ndi kuthira muulimbo pouphika. Zotsala pafunika kubviika m'madzi pamene munthu afuna kuchera mbalame. Patapita nthawi zonsezi zibvuulidwe ndi kuyanika

padzuwa, ndipo nthawi yomweyo mbalame zidzauma kukhosi ndi kumva ludzu, ndipo zidzabwera zambiri ndi kutera pa mitepa ya ulimbo. Tsono apo munthu akhoza kugwira mbalame zambiri.

Zinziri (Mbalame)

Palibekanthu ndi.
Chiumi.

Machitidwe : Kusokoneza zonsezi ndi kumakhulira ku zingwe zache za msampha. Zinziri zidzaumirira kubwera ku msamphawo ndipo zikhoza kugwidwa pa msamphapo.

Uzimba

Zala za Kamtema,
Zala za Kamphambe ndi
Zinyatsi za m'malunje.

Machitidwe : Zina zifunika kutentha ndi kutemera m'manja. Zina zifunika kusokerera nsalu ndi kumanjata padzanja, kupanga njirisi. Zina zifunika kulonga m'bano la mpaliro. Munthu akachita izi adzakhala osodza.

Goba (Deka)

Nsomphole,
Chibzero ndi
Mtsiroti.

Machitidwe : Pokonza mkombero wa goba pafunika kuika mankhwala amenewa mumkomberomo ndipo mbewa zambiri zidzathamangira m'goba amene'yu-

Inswa

Madzi amatalala osungunukira mchipala,
Gaga wachimanga.
Namchigaga ndi chabzyero.

Machitidwe : Zonsezi zifunika kubviika m'madzi ndi kumathira madziwa mu minyawa ya inswazo. Namchigaga ndi Chabzero zifunika kusesera mlitala la inswazo ndi kumatsitsira dothi ndi zinyatsi mu mtsuko mwa litala. Zitatha izi inswa zambiri zidzalumbira.

Malonda

Nsomphole,
Chinyatsi cha pa msika,
M'petu ndi Palibe kanthu.

Machitidwe : Zonsezi pafunika kuzitentha ndi kumafutira phulusa lache m'mene muli zamalonda. Malonda adzagulidwa koposa.

Mwayi wa Nchito

Kanthu kali mwai (Kachirombo kofanana ndi gonondo)
Palibekanthu ndi
Mwanjano.

Machitidwe : Zonsezi zifunika kuzisokera msalu kupanga njirisi ndi kumanjata padzanja nthawi zonse. Munthu pofuna nchito adzaipeza msanga ndiponso mwini nchito adzamkonda koposa.

Mirandu (*Untherera*)

Mleza,
Ndebvu za Khoswe,
Ndere za m'madzi,
Makwa (Mamba) a Nsomba ndi
Mtengo wa nkhwichi.

Machitidwe : Zonsezi kuzisokera m'nsalu kupanga chithumwa (njirisi), ndi kumanjata padzanja. Nthawi zina pafunika kubviika m'madzi njirisiyo ndi kumasamba m'maso madziwo kuti munthu akhale ochangamuka ndi ochachuka pokamba nkhani zachezo, motero kuti sangamutsutse pa mirandu.

9. *UBWANA NDI UNAMWALI*

Ana a Kalikokha ndi Dambudzo panthawi zonse zimene anali kusewera anali kuyimba nyimbo zosiyana-siyana. Masewera amenewa anali kuchitika nthawi za madzulo mwezi utawala. Nthawi za midima masewera sanali kuchitika kawiri-kawiri. Nyimbo zimenezi nthawi zinanso zinali kuyimbidwa kumadambo, pa mitondo, ku mapiri ndi ku malo ena ambiri. Anawa anali kuchitanso ndakatula zina zambiri zina zinali zotere :—

(1) *Wadya umba*

Wadya, wadya umba,
Umba, umbatole,
Tole, tole kwakwa
Kwakwa, kwakwa mbiri,
Mbiri, mbiri yezi,
Yezi, yezi noko,
Noko, nokolera.

(2) *Waphanji ?*

Galu wapha Bakha,
Bakha wapha Galu,
Bakha wapha Galu,
Galu wapha Bakha.

(3) *Birimankhwe leke*

Birimankhwe, birimankhwe, lek'undiruma,
Birimankhwe, birimankhwe, chimlomolende !

(4) *Kamtungulu*
Kamodzi, kawiri, kalizamtungulu,
Jere, magombo, jikijira, malire, nteregu !

(5) *Tondolo*
Tosi, tondolo, beka, masamba,
Piripiti, kamlomo, kwanyali,
Zalira, zintole, lipumi.

(6) *Kamtsine*
Kamtsine, kamtsine, kamtsine-tsine,
Tsinibulu, tsinibulu !
Tsinibulu ! !

(7) *Njala ya mto-to-to-to*

Mtsogoleri : Tambalale ! D.C.
Onse : Ya-ya-ya ! D.C.
Mtsogoleri : Namkamwini phikani gaga,
Akadye akumunda, kumunda,
kuli njala yamti-ti-ti-ti,
Funya mwendo !

(8) *Chimwezi Chakumwamba*

Mtsogoleri : (*a*) Chimwezimwezi ye ! D.C.
Onse : Aye ! D.C.
Mtsogoleri : Nakamunawo akhale pansi chakumwamba !
Onse : Aye !
(*b*) Chimwezimwezi ye ! D.C.
Aye ! D.C.

Nachimbalanga akhale pansi chakumwamba !
Aye !

(9) *Tsekulire*
Namwali tsekulire
Namwali tsekulire a-e-a-ya-e-e-e !
Ana awa a-e-a-ya-e-e-e !
Ine mnuwake a-e-a-ya-e-e-e !
Kum'puta dala a-e-a-ya-e-e-e !
Ndidya timbingu
(timphutsi) a-e-a-ya-e-e-e !

(10) *Msendekele Limadzi*

Mts. : Ndikuti ndikuti msendekele ndiulimadzi ! D.C.
Onse : Msendekele !
Mts. : Ndiwo m'kadule msendekele ndi'ulimadzi ! D.C.
Onse: Msendekele !

(11) *Nsingakwe*

Mts. : Nsinga kwe-kwe-kwe nsinga ! D.C.
Onse : Kwe-kwe-kwe !
Mts. : Tione wolimba uta de !
Onse : Pansi mpanyama !

(12) *Adula Tonde*

Mts. : Adula tonde ! D.C.
Onse : Nadule !
Mts. : Nanga apa ?
Onse : Ai-ai pali mwana wakhanda !

(13) *Choso*

Mts. : Adapita tong'o ! D.C.
Onse : Adabwera adadzaona ana !
Mts. : Tong'o-tong'o D.C.
Onse : Adabwera adadzaona ana !
Mts. : Choso — choso D.C.
Onse : Adabwera adazaona ana !

(14) *Nthudza*

Mts. : Tikadye nthudza !
Onse : Zidapsya !

(15) *Chirondola*

Mts. : Kalondolondo, kalondolondo,
Kalondola nkhonda Ajere ! D.C.
Onse : Kalondola !
Mts. : Ndi amuna ao kalondola nkhondo Ajere !
Onse : Kalondola !
Mts. : Adapita muno kalondola nkhondo Ajere !
Onse : Kalondola !

(16) *Chirondola Mbalame*

Mwana wambalame usaululuka
Nkudulu mapiko D.C.
——Ndaululuka ndekha ! (wobisala)

(17) *Kadzidzi*

Hi-hi !

Alirayo kang'ono mumtayire ! D.C.
Uyo nkadzidzi !

(18) *Kauye*

Kumwamba kuli a Kauye !
Kauye — Kauye !

(19) *Mbulumbunde*

Mbulumbunde mtama !
Adum'mana m'tokhoswe !

(20) *Chuwa*

Mts. : Chuwa — chuwa — chuwa !
Onse : Tikone madzi ku mchenga !

(21) *Liwiro*

Mts. : Liwiro !
Onse : Lampombwe !

(22)

Mts. : Jo ! Jo ! Jo !
Onse : Jowa !
Le-e-e-e !
Jo-o-o-o !

(23) *Nyumba Iyi*

Mts. : Nyumba iyi njayani !
Njamkazi kuwalika,
Tendeni tiwalike !
Onse : Waliku ! waliku !

Mts. : Nyumba iyi njayani ?
Njamkazi kufendeza,
Tendeni tifendeze !
Onse : Fendezu ! ——— fendezu !

(24) *Phere-Phere*

Phere-phere m'pamnyendo,
Mkhomo m'pitamu,
N'ocha mbatata yanga pa motopa,
Wogo, ija yapsyerera.
Tadzaocha ina mawa.

(25) *Mwezi Ukawala*

Mts. : Kamaoya — oyae !
Yę-ye-ye !
Kamaoya — oya-e — woye !
Onse : Mwezi ukawala !

(26) *Chitute*

Mts. : Chitute : Chitute !
Onse : Angomatola malo naika msenjere !
Chitute-e-e-e sichingadze chokuona.
Mts. : Mmawa-a-a-a !
Onse : Natuta-a-a-ą !
Mts. : Msana-a-a-a !
Onse : Natuta-a-a-a !
Mts. : Madzulo-o-o-o !
Onse : Natuta-a-a-a !
Mts. : Chitute-e-e-e !
Onse : Sichingadze chokuona.

(27) *Maso Adachitabwanji*

Mts. : Birimankhwe ! Birimankhwe !
D.C.
Maso adachita bwanji ?
Onse : Kwathu Kwayera msamaseka ana inu !
Mts. : Ine n'dzachoka.
Onse : Ine n'dzachoka pam'dzi pano.
Mts. : Mukhale m'mange !
Onse : Mukhale m'mange pam'dzi pano.
Mts. ndi Onse : Taonani kukhomokwangaku,
Kwayera mbe-e-mbe-embe-e-e !

Mafuta akale amene Dambudzo anaonetsa ana ache ndi awa :—

Mafuta a nsatsi, bombwe, linale (ochokera kumitengo), ndipo mafuta a nyama ndi nzimbe. Dambudzo anawaonetsanso ana ache zobvala zina zodzikometsera nazo zotere :—

Chambato = Chobvala mkhosi cha mkanda.
Chiringondi = Chobvala chiwondo kuyambira m'chuuno mpaka mnchafu, koma chothekera mikanda.
Chithenera, Chithimbamero, Kamiza = Mkanda wobvala mkhosi koma chambato chinali ndi khwakhwa.

Ndalira	= Chikono (chachitsulo) makangala.
Zimphusu	= Zinchoto zobvala m'manja ndi mmiyendo (ndungunya)
Chiwewe	= Nsangamutu yokongola.
Nsolokoto	= Zobvala kumwendo ngati mkanda.
Chiphimbi	= Chobvala chachikopa chobvala kumaso kokha.
Katapa	= Chobvala cha mkanda choika kunkhongo.
Mtiza	= Mkanda wakale, majuguja, lanje, gobede, kulale.
Zipote	= Mkanda wobvala ena akuti mapweremwe, zinganga, sabiri, chuma, magida, zipotera, chigwetsera, seza.

Dambudzo anaonetsanso ana ache zakudya zakale monga izi :—

Mchewere, mapira, kansinsi, khobwe, kambulunje, (monga nzama) chinkhubwa, ndi chimanga. Anapitiriza ndikuwaonetsa zolimira zakale monga izi :— gowo (khasu la mtengo), nsunsi (khasu lachitsulo la mtapo wa nthale).

Dambudzo analongosola zonse zamakometsero (mphini) a zamthupi mwachidule motere :—

Za Kumaso ndi Mmasaya

Chitopole
Konde
Kanjedza
Mapazi anjiwa
Nkhunyukunyu
Kamata
NKholosa/Mchomi
Mafuwa a chitopole
Maunikira (matsunyulira)
Matambira

Za Pamimba

Ch'angatamchombo
Zunguliramchombo
Chidyamwini
Chithatha
Bonde
Makhonya
Kooche
Gonampini

Za Mmiyendo (Mnthanthula

Ndale
Tsate kukudere
Chiona alongo
Chiona ankhoswe

Za Pamtima

Tsetsende, Khumbo, Kulusa — Za pakati pa maere. (za pakati pa maere)
Magwanda (za pakati pa maere)
Chigwera maere (Za mmunsi mwa maere)
Chitengamtima
Kwenje

Za Kumsana

Atina
Njale
Chithyolaulendo
Mlamundiphate
Mkwenyabwerani
Katsekechitseko
Tseka ubwere

Za Mnchafu

Matipa
Chiotheramoto
Nembo
Maso

Za Mmanja
Macheka
Kapereke Nsima
Kapereke Madzi
Mtsamiro

MAFUNSO

1. Chiipirawachaje anafotokoza za mwambo wa Chokolo, kodi inu muli ndi malingaliro otani pa Chokolo ?
2. Phulantenga ndi Zingalume anadziwa nchito zotani ? Chulani zisanu zokha.
3. Kodi matanthauzo a mau awa n'chiyani ? : Nsala, chiridzo, phodo, kauli, ngolowodza, nthera, mubvi, ngombe, mkuzi, kapena mpango, kachesa.
4. Kodi Dambudzo ankauza ana ache mwambo wotani kuti azikhala okongola ?
5. Fotokozani mitundu yonse ya zobvala zakale monga adanena Dambudzo.
6. Nanga i'zi n'ziyani ?
   Chithimbamero, majuguja, mapweremwe, ngayo, lanje, makangala, chambato, chithyolaulendo, njereka, nsunsi.
7. Lembani pena werengani mawerengedwe akale a *Tekiteka* pena a *Kamba.*
8. Chulani pena Lembani mtundu wa zakudya zisanu zakale.

9. Lembani maina a mphini mwa chirongosoko ichi :—
   (*a*) Maina anai za kumaso ndi mmasaya.
   (*b*) Maina anai za pamtima.
   (*c*) Maina atatu za pamimba.
   (*d*) Maina atatu za kumsana.
   (*e*) Maina awiri za m'nthanthula (m'katumba)
   (*f*) Maina awiri za mmikono.
10. Kodi Dambudzo anapangitsa ana mankhwala achikondi motani ?
11. Fotokozani mwachidule mmene Kalikokha analongosolera za mankhwala a mangolomera ndi ophera inswa.
12. Lembani nyimbo ziwiri pa izi :—
    (*a*) Choso.
    (*b*) Chitute.
    (*c*) Adachita bwanji ?
13. Lembani magule asanu a chigawo chapakati cha Malawi ndi asanu amene Kalikokha adakaona ku chigawo chakumwera.
14. Kodi zoimba-imba ziri magulu angati ? Perekani zitsanzo zisanu pa gulu liri lonse.
15. Chulani mitundu isanu ya misampha.

10. *MAPHUNZIRO AKALE*

Ana a Kalikokha ndi Dambudzo analandira maphunziro a zinthu zina ndi zina zambiri.

Akazi ndi Amuna

Kalikokha masiku ambiri anali kunena mau motere: " Ana inu, muyenera kudziwa kuti ana amuna ndi akazi safunika konse-konse kukhalira pamodzi. Amuna azikhala kwaokha ku mabwalo ndiponso akazi ku mitondo. Mkazi amene akhala kwekwenu-kwekwenu ndi amuna kaya ndi akazi ameneyo ndi chitsiru."

Kalikokha anapitirira ndi kuti: " Ana inu, tsopano, muyenera kudziwa zambiri monga za uzimba, zaluso, kuumba mbiya, kulima minda, kuyimba, kusema zosema, kusinja moyenera, ndi kuphika zakupsya !"

Dambudzo anapitirira ndi kukamba ndi ana ache nati: " Anamwali inu, tsopano muyenera kumabvala moyenera, osamabvala kazimeso ai, ndiponso osamabvala nsalu yogauka-gauka ai, izi zichotsa ulemu wa munthu."

Kalikokha anapitirira kuphunzitsa ana ache nati: " Ana inu, muziyenda mochenjera. Kudziko kuno kuli anthu akaduka ndi azao kotero kuti amatha kuwachitira mankhwala kuti apeze tsoka. Mwina

amachita mankhwala opundula anzao, mwinanso kulodza anzao. Kuti mulewe zonsezi pafunika kuti nonse'nu ndipite nanu kwa a Sing'anga ena amene amadziwa mankhwala a thupi, ochinjiriza ku mankhwala oipa. Tikatero, inu simudzapeza tsoka pa moyo wanu lochokera kwa munthu mnzanu." Onse aja anawachitira mankhwala monga adawapangira.